# Kodi Makwaya Amu Mpingo Ndi Mayimbidwe Zicokera M'malemba?

Ambiri agwiritsa makwaya ndi mayimbidwe mukuyesa kupembedza Mulungu. Kodi Mulungu alola ma kwaya ndi mayimbidwe mu cipembedzo ca ci Kristu? Kuti tipeze yankho ku funso lotere, tiyenera kusanthula mu Baibolo. Baibolo ndilo liu la Mulungu (2 Timoteo 3:16, 17; Yohane 12:48; Agalatiya 1:6-9; 2 Petro 1:3; Yuda 3). Munthu alibe mphamvu ya kuonjezera kapena ku cotsako ku ciphunzitso ca Mau a Mulungu (Cibvumbulutso 22:18, 19: Deuteronomo 4:2; Miyambo 30:6). Gawo la Cipangano Catsopano ca Mau a Mulungu ndi limene muli malamulo apa nchito ndi cipembezo ca Mulungu cimene ticita (Akolose 2:14; Ahebri 8:6-13).

Mu Mau ace Mulungu analamulira zinthu zisano mu cipembedzo ca mu Mpingo wace. Zinthu zisano ndi izi: Kuyimba (Aefeso 5:19; Akolose 3:16), Kupeleka - (1 Akorinto 16:1-2; 2 Akorinto 9:6, 7), Pemphero - (1 Atesalonika 5:17; 1 Timoteo 2:8), Kudya Mgonero Wa Ambuye - (1 Akorinto 11:23-29; Macitidwe 20:7); ndi Kulalikira Mau a Mulungu (Macitidwe 2:42; 20:7; 2 Timoteo 4:1-4). Zinthuzi za cipembedzo zilamulidwa mukulankhula, mukulamulira, mukusonyeza ndi muzisanzo zololedwa. Kuyimba mu cipembedzo kulamulidwa ndi Mulungu. Mu Cipangano Catsopano muli zisanzo zambiri za Akristu oyimbira Mulungu mu cipembedzo (Macitidwe 16:25; Aroma 15:9; 1 Akorinto 14:15; Aefeso 5:18-19; Ahebri 2:12; Yokobo 5:13). Awa malemba atiuza mayimbidwe m'mene Mulungu alamulira anthu ace m'mene ayenera kumlambira mu mzimu ndi m'coonadi (Yohane 4:24). Mayimbidwe amene Mulungu analamulira ndi, kuyimba. Kuyimbaku ndi kwakuti mpingo onse uyimbe panthawi imodzi. Akristu onse amene asonkhana ayenera kuyimbako! Kuyimbaku kuyenera kucitika ndi cidziwitso. Colinga coyimbira ndi cakuti Akristu alemekeze Mulungu ndi kuphunzitsa ndi kudzilankhulira eni okha.

**Kodi Cipangano Catsopano ciphunzitsa Mayimbidwe a Mpingo onse?** Kodi Aefeso 5:19 iphunzitsa mayimbidwe a Mpingo onse? Liu la m'cilankhulidwe ca Mcihelene mumene Cipangano Catsopano cinalembedwera, cimene anatanthauza kuti "kulankhula," kutanthauza kuti "kutulutsa mau, kupeleka mau, kugwiritsa lilime kapena kutulutsa mau, kulakhula, kuudza, kugwiritsa mau ochokera mu maganizo a munthu." Liu la M'Cipangano Ca Tsopano lotanthauzidwa "nokha" ndi liu litanthauza unyinji wa anthu. Kutanthauza kuti muntu wocitayo ndi wolandira ndi m'modzi. Monga kuti, pamene wina alankhula kwa ena ndi ma salmo, ndi mayamiko, ndi nyimbo zauzimu, ena ali kulankhulanso kwa iye cimodzimodzi. Uku ndiko kuyimba kwa mpingo wonse kumene osonkhanawo aphunzisana wina ndi mzace pomangilizana mau awo pamodzi mu nyimbo. Kutsatira lamuloli, kuyenera kuti kukhale kuthandizana mukuyimba. Pamene gulu la anthu kapena munthu umodzi woyimba (monga Kwaya ndi woyimba umodzi) ayimbira (gulu lina limene lingomvetsera monga Mpingo), pakhala palibe kuthandizana m'mayimbidwe motero kuti Aefeso 5:19 siigwirizana nayo Kwaya kapena woyimba m'modzi!

**Kodi Akolose 3:16 iphunzitsa Mayimbidwe a Mpingo onse?** Liu la M'Cipangano Ca Tsopano lotanthauza "kuphunzitsa" litanthauza "kuphunzitsa, ku langiza ndi pakamwa." Cifunikira kuti iye wophunzitsidwayo amvetse ciphunzitsoco. Liu la M'Cipangano Ca Tsopano lotanthauzidwa "kuyambirirana" itanthauza kuika m'maganizo, kulangiza, ndiponso kucenjeza." Kuphunzitsaku ndi kuyambirirana kuyenera kucitikira mwa "eni okha." Liu "eni okha" M'Cipangano Ca Tsopano litanthausa "nokha" monga mu Aefeso 5:19. Chifikea cace, pamene Mpingo uli kupembedza Mulungu mu mayimbidwe, pakhala kuphunzitsa ndi kuyambirirana eni okha. Akolose 3:16 iphunzitsa mayimbidwe a Mpingo onse! Pamene kagulu kapena munthu m'modzi (Kwaya kapena m'modsi woyimba) ayimba tsono mpingo umvetsera cabe pakhala palibe kuphunzitsana kapena kuyambirirana!

Mayimbidwe a Mpingo onse ndiyo inali njira yokha yotamandilamo Mulungu pa ciyambi ca Mpingo. Koma anthu ambiri lero akamba kuti Makwayo ndi mayimbidwe ali ololedwa mu mpingo cifukwa Baibolo si ikambako kanthu kali konse pa za mayimbidwe otere. Pamene Mulungu anapeleka lamulo kwa Akristu kuti ayenera kuyimba ndi kuyambirirana eni okha, kutero Mulungu anacotsapo makwaya kapena mayimbidwe ena ace M'cipembedzo cace. Sicinali cofunikira kwa Mulungu kupeleka ndandanda woti "Usayimbe motere." Mulungu sanali kuyenera kukamba kuti, "Usalize zilimba kapena zitoliro poyimbira ine mu cipembedzo canga." Sicinalinso coyenera kwa Mulungu kunena kuti, "Usayimbe ma Kwaya kapena kuomba m'manja m'cipembedzo canga." Pamene Mulungu anati muyimbe nonse mu mpingo, kutero

kunali kucotsako makwaya ndi mayimbidwe onse amene Mulungu sanalamula monga kuomba m'manja poyimba, kuliza lipenga, zisakasa, azeze, malingaka, zoyimbira za zingwe ndi zitolilo polemekeza Mulungu.

M'Cipangano Ca Tsopano Ambuye sanalole makwaya kapana mayimbidwe adzitsulo zoyimbira! Kunalibe Mtumwi wa Kristu amene analola makwaya ndi mayimbidwe oterowo mu cidembedzo ca Mulungu. Kunalibe Mlembi wa M'Cipangano Ca Tsopano amene ana phunzitsa kapena kulola mayimbidwe ama Kwaya mu cipembedzo ca Mulungu. Kulibe cisanzo ciri conse ca mayimbidwe amakwaya ndi mayimbidwe azolizaliza kapena kuomba m'manja poyimbira Mulungu mu cipembedzo cace M'cipangano Ca Tsopano. Cifukwa cace ndi zosaloledwa ndi Ambuye! Kudzigwiritsa nchito mu cipembedzo ndi ucimo (Mateyo 15:8, 9-12; 2 Yohane 9-11; Cibvumbulutso 22:18-19).

### Kodi Cipembedzo ciyenera kukhala cotsangalasa anthu?

Ambiri aganizira tero. Akristu ayenera kudziwa kuti Mulungu analamulira kumlambira mu *"mzimu ndi m'coonadi"* (Yohane 4:24). Ici citanthauza kuti Mkristu ali yense ayenera kupemphera ndi mtima woona ndi zicitidwe zabwino zokondweletsa Mulungu. Mulungu ndiye amene apembedzedwa cifukwa cace tiyenera kukondweletsa Mulungu osati anthu ai.

### 1 Akorinto 14:26

Anthu ena ayesa kucinjiliza ma kwaya ndi mayimbidwe pokamba kuti 1 Akorinto 14:26 iphunzitsa zotere. Mukayanganitsitsa vesi limeneli mudzaona kuti si ili kuphunzitsa zimenezi za makwaya kapena mayimbidwe. Kukamba kuti, *"yense ali nalo salmo"* sicitanthauza kuti ali yense anayimba nyimbo yace kapene kuti ambiri anayimba nyimbo zawo. Salmo ingangowelengedwa kapena kuculidwa Mukaletayi, Paulo afotokoza zakusagwiritsa bwino mphaso za uzimu. Kalongotsedwe kabwino katanthauzo la vesi limeneli kali M'Macitidwe 4:23-30. Ndipo m'mene ophunzira adamva zimene zinacitika kwa Petro ndi Yohane *"anakweza mau kwa Mulungu ndi mtima umodzi"* (Macitidwe 4:24).

### Mbiri Ya Mpingo

Lyman Coleman, Mlembi wa mbiri ya mpingo, anelemba kuti, "Mayimbidwe amu Mpingo pa zaka mazana atatu oyamba anali amu Mpingo onse. Mpingo onse unali kuyimbira pamodzi nyimbo zotamanda Mulungu. Amuna, akazi ndi ana anali kuyimbira pamodzi nyimbo zotamandira Mulungu mu Mpingo" (*Ancient Christianity Exemplified*, tsamba 329, 330).

Kulambira kuli konse, pa nthawi zonse, ndi pa malo onse kuyenera kucitika mu mzimu ndi m'coonadi (Yohane 4:24). Ngati munthu salambira ndi macitidwe abwino ndi mtima wabwino munthuyo cipembedzo cace ndi ca cabe ndiponso ali wocimwira Mulungu. M'Cipangano Ca Tsopano mulibe lamulo limene libvomereza ma Kwaya Ndi Mayimbidwe mu Mpingo. Motero kuti amene acita zimenezi ali mkulambira mwa cabe ndiponso ali ndi ucimo kwa Mulungu.

*Truth For The World*

truthfortheworld.org

info@tftw.org

P.O. Box 241
Bethel Springs,
TN 38315 U.S.A.



Kodi

# *Makwaya Amu Mpingo Ndi Mayimbidwe*

# ZICOKERA M'MALEMBA?